**ttb_Nya_0838_script**

**2 Atesalonika : 2:7-17**

**Mutu : Kubwera kwa Wokana Khristu (Antichrist)**

Ndipereka moni kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tiyeni lero Ambuye atitsogolere ndi mau ake apa 1 Petro 3:10, akuti, “Iye wofuna kukonda moyo, ndi kuona masiku abwino, aletse lilime lake lisanene choipa, ndi milomo yake isalankhule chinyengo.”

Tsono mupologalamu yapita ija, tinali kukambirana pa 2 Atesalonika 1:10-2:9, nkhani ya Tsiku la Ambuye. Ndiye lero pa 2 Atesalonika 2:7-17, tiona nkhani yakubwera kwa wokana Kristu (Antichrist).

7. Pakuti chinsinsi cha kusayeruzikachayambadi kuchita, chokhachi pa womletsa tsopano, kufikira a kam’chotsa pamenepo.

M’chitidwe wakusaweruzikakudayamba nthawi ya Paulo ndipo ukupitilira lero lino. Ambuye Yesu adaphunzitsa kudzera m’fanizo limene limawonetsanso momwe dziko lapansi liliri lero lino.Zinsinsinsi za Ufumu wa Kumwamba zimabvumbulutsa momwe dziko lapansi liriri. Mau a Mulungu akufesedwa masiku

ano koma m’dani naye akufesanansongole.Tirigu ndi nansongoleakumelera pamodzi.Mau a Mulungu ndi nansongoleakukulira limodzi lero lino pa dziko lapansi.

Tsono kusaweruzika kukhala kukupitirirabe, koma Mzimu Woyera sakumulora Satana kuchita chifuniro chake chosaweruzika.Koma Mzimu Woyera akadzamulora Satana kuchita chifuniro chake pamenepo Satana adzamasuka kuchita kusaweruzika m’dziko lapansi.

8. Ndipo pamene adzabvumbulutsidwawosayeruzikayo amene Ambuye Yesu adzamuwononga ndi mzimuwa pakamwa pake, nadzamuwononga ndi mawonekedwe a kudza kwake.

Tsono pamene adzabvumbulutsidwawosayeruzikayoadzakhala wopanda womutsutsa padziko lapansi.Ambuye Yesu yekha akadzafika ndi amene adzamugonjetse. Monga ana a Isreali anali pamasautsoakulu ku Aigupto ndi momwenso okhulupiriraadzakhalire pansi pa ulamuliro wawosaweruzika wokana Khristu. KudzakhalaChizunzo kufikira Yesu atabwera kudzakhazikitsa ufumu wake.

Ambuye Yesu adzamuwononga ndi mzimuwapakamwa pake: Kutanthauza kuti Ambuye adzamugonjetsa ndi Mau ochokera pakamwa pake amene ali ngati lupanga lakuthwakonsekonse. Ndi Mau a Mulungu amene adalenga dziko lapansi. Mau a Mulungu ndi Malemba a moyo amphamvu.Ambuye Yesu pobweraadzabwera ngati Mau a Mulungu amoyo.

“Nadzamuwononga ndi mawonekedwe a kudza kwake.”Mawonekedwe a kudza kwake kutanthauzaulemelerowa kubwera kwake. Pa Tito 2:11 akunena kuti: “Pakuti chisomo cha Mulungu chimene chibweretsa chipulumutso chawonekera kwa anthu onse.” Kubwera kwake mu ulemelerokudzakhala kudzatenga okhulupirira kudzakhazikitsa ufumu wake. Anadza ku Betelehemu ngati mwana wakhanda, ndikuyamba utumiki wake ali ndi zaka makumi atatu pamene adapitandikuyeretsakachisi. Pobweranso kachiwiri adzabwerakoyambirira kukumana ndi mpingo wake mu mlengalenga ndipo pomalizaadzakhazikitsa ufumu wake. Panthawi imeneyo okana Yesu adzawonongedwa ndi mawonekedwe a kubwera kwake.

9. Ndiye amene kudza kwake kuli monga mwa machitidwe a Satana, mu mphamvu yonse, ndi zizindikiro ndi zozwizwa zonama.

Paulo pano akukamba za munthu wauchimo, wokana Khristu, munthu wosaweruzikawamachitidwe a Satana mu mphamvu yonse ya zizindikiro ndi zozizwa zonama.Munthu wosaweruzikayu adzakhala ndi mphamvu zodabwitsa monga kuchilitsa matenda.Kumbukirani kuti nthawi ya Yobu Satana adatumiza mphepo imene idapha ana a Yobu psiti.Satana adzabwera ndi mphamvu ndi zozizwa. Pachifukwa ichi sitiyenerakuyika chikhulupiriro chathu pa anthu koma pa Yesu Khristu amene ndi woyamba ndi wotsiriza wa chikhulupiriro chathu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsindike pa mau akuti, munthu wosaweruzikayuadzafikandizizindikirozachinyengo, zonamiza anthu.Anthu pa dziko lonse lapansi adzayamba kukamba za munthu wosaweruzikayu.Anthu amene sakhulupirira Uthenga Wabwino adzakhulupirirazachinyengo ndi zonama za munthu wauchimowosaweruzikayu.

10. Ndi m'chinyengo chonse cha chosalungamakwa iwo akuononongeka, popeza chikondi cha choonadi sanachilandira, kuti akapulumutsidwe iwo.

"Ndi m'chinyengo chonse cha chosalungama kwa iwo akuononongeka" Munthuwosaweruzika adzachita kusaweruzika kwake kudzera mwa anthu amene akuwonongeka. Anthu enaakuwonongeka chifukwa safuna kulandira chowonadi kuti apulumutsidwe.Uthenga Wabwino ukulalikidwa ndipo tsiku lina udzafikira dziko lonse lapansi. Ngakhale palimadera ena kumene amakana mpingo ndi alaliki sangathe kufikako,komabeuthengawuukufika mwa njira zina monga kudzera pa wailesi. Tsono alipo amene amamva Uthenga Wabwinowu koma amaukana.Anthu oterewa akukana kulandira chowondadi.

Nkhani ikunena kuti chinyengo chonse chosalungamachimachitika ponamiza amene akuwonongekawo ngati akuchita zinthu zolungama.Chinyengo chosalungama chili ndi mawonekedweachilungamo.Chitsanzo chachinyengondichiphunzitso chakuti munthu akapulumutsidwa chifukwa chochita ntchito zabwino.Anthu amene amanyengedwa

ndi chiphunzitso chonama ichi akuwonongeka kotero kuti amanyengedwa ndi chikhalidwechachipembedzo koma chokana mphamvu ya Mulungu.Anthu ena amapembedza mafano, ena amapeza mphamvu yamapemphero kudzera ku zinthu zina, mwina kupemphera kudzera mwa anthu akufa, poganiza kuti akatero akhoza kupeza chisomo pamaso pa Mulungu. Uku ndikudzinyenga chabe ndipo anthu otere Satana adawaphimba maso kotero kuti Uthenga Wabwino umawoneka ngati chopusakwa iwo chifukwa akuwonongeka.

Anthu awa akuwonongeka chifukwa sanalandire chowonadi.Chowonadi chimachokera kwa Mulungu mwa Mzimu wa chowonadi. Kukana kulandira chowonadindikukana kulandira Mulungu Atate wachowonadi, Yesu amene ndi Chowonadi ndi Mzimu Woyera wachowonadi. Kukana Mulungu ndikokusankhachiwonongekakosatha.

11. Ndipo chifukwa cha ichi Mulungu atumizakwa iwo molimbamachitidweakusocheretsa, kuti akhulupirire bodza.

Mulungu amawalekelera anthu okanachowonadi kuti akhulupirire bodza.Funso nkumati kodi Mulungu amachitiranji zimenezi? Anzanga tamverani! Mulungu adalimbitsa mtima wa Farao yemwe

sizimamukhudza kuti ana a Israeli akuzunzidwa. Mulungu adamulimbitsa mtima kotero kuti sanafune kuti ana a Israeli atulutsidwe mu ukapolo kwa Aigupto. Mulungu adachita zimenezi kuti Farao apange chiganizo kapena chisankho.Koma monga anthu ambiri lero safuna kupanga chisankho ndipo zotsatira zake Mulungu amawapangitsa kuganiza zinthu zolakwika chifukwa anthuwo akana kulandira chowonadi. Mulungu amawalankhulam'Mau ake ndipo iwoamakana kukhulupirira.

Anzanga, anthu amene adasiya kupita kutchalichi kumene kumalikidwachowonadi amakhala pachiwopsezochokhulupirira ziphunzitso zabodza zimene masiku ano ziliponseponse.Ena mwa anthu amenewa akupita m'makomoya anthu kufanafuna anthu akuti awasokeze ndi mabodza awo.Amadziwa kuti anthu okanachowonadi sapita kutchalitchi ndipo amawalondola pa njira ndi m'nyumba zawo.Anthu amene salandira mau a Mulungu, kotero kuti amatsegulirakhomo chikhulupiriro chabodza.Chomvetsa chisoni ndichakuti alipo anthu a nzeru amene amakhala mtchalitchiadamvaUthenga Wabwino koma adaukanandikutsata chikhulupiriro chabodza. Amanyengedwa ndi

anthu otayika,okana kulandira chowonadi.Anthu otere amakhulupirirabodza.

Tsono ino, ndiyo nthawi yomwe Mulungu akulekanitsa nkhosa ndi mbuzi.Mulungu amalora anthu amene akana kulandira chowonadi kuti akhulupirire chinthu cholakwika ndipo amakhulupirira chinthu chabodza.Bodza la wokana Khristundilakuti Yesu Khristu si Ambuye, ndipo Yesu amanama kuti ndi Mulungu.Wokana Khristuamawapangitsa kukhulupirira kuti chikhristu ndi chinthu chopusa, chikhulupiriro cha anthu opanda nzeru. Iye, amapusitsa anthu ndi malingaliro awo owoneka a nzeru kwa anthu amene akuwonongeka. Anthu amene akuwonongekaamakhulupirirabodza limeneli osazindikira kuti akulowa mu nyengo ya Chizunzo Chachikulu.

12. Kuti onse awonongeke amene sanakhulupirire choonadi, komatu anakondwera ndi chosalungama.

Mulungu adzaweruza anthu amene akukana chowonadi.Anzanga mukhoza kukhala kuti mumawerenga Mau a Mulungu ndikumvetsera Mau a Mulungu, koma ngati simukhulupirira kuti mau a Mulungu ndichowonadimudzakhulupirira chinthu

cholakwika.Kusakhulupirirachowonadindikutsegulakhomo kuti chikhulupiriro cha bodzachilowe mumtima mwanu.Ndiye tikunena kuti inu, mukasowa chowiringula pamaso pa Mulungu ngati simulandirachowonadi lero mwayi mukadali nawo.Ndikudandaulireni kuti musatsegulirekhomo chikhulupiriro cha bodza chifukwa simukufuna kulandira chowonadi.Inutuchowonadimwachimva ndipo ndikhulupirira kuti mudachimvakambirimbiri. Koma funso ndilakuti kodi mudalandiraChowonadi amene ali Yesu amene akakufikitseni pamaso pa Atate wake? Tamvani Paulo pa 2 Akorinto 2:15-16 akuti; “Pakuti ife ndife pfungo labwino la Khristu, kwa Mulungu mwa iwo akupulumutsidwa, ndi mwa iwo akuwonongeka; Koma kwa ena fungo la imfa ku imfa; ndi kwa ena fungolamoyo ku moyo. Ndipo azikwanira ndani izi?”Kutanthauza kuti inu, mukamukana Yesu Khristu ndiye kuti mukulandirafungolachiwonongeko, imfa.Koma ngati mulandira Yesu Khristu ndiye kuti mwakhulupirirachowonadi ndipo Yesu akulonjeza moyo wosatha.

Ndiyemkhristuazikhalam’moyo wosonyeza chikhulupiriro chachiyembekezo chakuti Ambuye Yesu akubwera.Kukhala ndichikhulupirirochachiyembekezo chakuti Ambuye Yesu akubwera

kumawonekera ndi zimene inu mumachita ndi Mau a Mulungu, mayendedwe anu komanso ntchito zanu.

13. Koma tiyenera ifetiziyamika Mulungu nthawi zonse chifukwa cha inu, abale okondedwa ndi Ambuye kuti Mulungu anakusankhani inu kuyambira pachiyambi, mulandire chipulumutso cha Mzimu ndi chikhulupiriro cha choonadi.

14. Kumene anaitanako inu mwa Uthenga Wabwino wathu, kuti mulandire ulemerero wa Ambuye wathu Yesu Khristu.

Tsono ndiyambe ndi mau akuti ndime ziwirizi, ndi zochititsa chidwi.Taonani zikukamba za nyengo ya kale, yatsopano ndi nyengo ya m’tsogolo.

a. Mulungu anakusankhani inu kuyambira pachiyambi: Monga Paulo adalembera m’buku la Aroma 8:28-31, pamene akuti: “Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizanakuwachitiraubwino, ndiwo amene aliwoyitanidwa ku cholinga chake. Chifukwa kuti iwo amene Iye adawadziwiratu, iwowa adawalamuliratuafanizidwe ndi chifaniziro cha Mwana wake, kuti Iye akakhale mwana woyamba

wa abale ambiri. Ndipo amene Iye adawalamuliratuwo, Iye adawayitana ndipo iwo amene adawayitanaadawalungamitsa,ndipo iwo amene adawalungamitsaadawapatsanso ulemerero. Ndipo tidzanena chiyani kuzinthu izi? Ngati Mulungu ali ndi ife, adzatitsutsa ndani?"

Paulo akulemba chimodzimodzi pa 2 Atesalonika 2:13 pamene akuti "Mulungu anakusankhani inu kuyambira pachiyambi."Pachiyambi ndi nyengo yakale.Inu ndi ine tikungoyenera kumva chimene Mulungu akunena ndikukhulupirira. Mwina funso nkumati: Ndiye mukutanthauza kuti Mulungu adandisankha ine ndisanabadwe? Tamvani a Dr. Spurgeon adayankhakuti "Amayamika Mulungu kuti adamusankha iye asanabadwe chifukwa akadadikira kuti abadwekayesakanamusankha ayi." Iye amatanthauza kuti sichikhala chinthu chodabwitsa kapena kudzidzimutsakwa Mulungu kuti inu mukhulupirirechowonandindikulandira Yesu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ikuti gakhale inu munasankhidwamusanabadwe, koma muyenera kudziwa kuti

inunso muli ndi chisankho.Tamvani Ambuye Yesu pa Yohane 7:37 anati;“Ngati pali munthu akumva ludzu, abwere kwa Ine, namwe.” Kutsimikiza kuti munthu aliyense mwakufuna kwake, adze kwa Iye mwachikhulupiriro. Amene sanabwerekwa Iye sichifukwa chakuti sanasankhidwe ayi, koma amaganiza kuti sakusowa chipulumutso. Kodi inu muli ndi ludzulofuna chilungamo, ndi chipulumutso? Bwerani kwa Yesu.

b. Paulo akunena kuti; “Mulandire chipulumutso cha Mzimu ndi chikhulupiriro cha choonadi.”Kutanthauza kuti muyenera kulandirachiyero. Kukhala woyeretsedwakumatipatsakuthekerakochita zinthu monga mwa Mzimu Woyera ndiponso kumatipatsa gawo m’banja la Mulungu. Kulandira Yesu ngati Mbuye ndi Mpulumutsi kumatiyanjanitsa ndi Mulungu. Kutsimikiza kuti kuyambira nthawi yomwe mudapulumutsidwa,nthawi yomweyomudayanjana ndi Mulungu. Tere tikunena kuti tikamayenda mwa Mzimu Woyera, timalandira chikhululukiro komansochiyero tsiku ndi tsiku. Ndipo poyenda mwa Mzimu Woyera timakula m’chisomo.

c. Ndiye pa mau akuti, “Chikhulupiriro cha choonadi Kumene anaitanako inu mwa Uthenga Wabwino.” Akutanthauza kuti

wokhulupirira ayenera kudziwa mau a Mulungu kuti akhozekukulam'chowonadi ndi m'chikhulupiriro. Izi, zikhoza kuchitika pamene inu mukhala ndi nthawi yowerenga mau a Mulungu.

d. "Kuti mulandire ulemerero wa Ambuye wathu Yesu Khristu." Nkhani ikuti, Ulemelerowa Ambuye wathu Yesu Khristu tidzalandira mtsogolo. Pa tsiku la mkwatulotidzakumana naye ndipo ulemelerowaKhristuudzawonekera mwa okhulupirira. Tamvani 1 Yohane 3:2, akuti, "Wokondedwa, tsopano tiri ana a Mulungu, ndipo sichidawoneke chimene tidzakhala. Tidziwa kuti, pa kuwoneka Iye, tidzakhalawofanana ndi Iye, pakuti tidzamuwona Iye monga alili." Ndipo Paulo polembera Akolose anatsindika kuti, "Kwa iwo amene Mulungu adafunakuwazindikiritsa chuma, chimene chiri chuma cha ulemerero wa chinsinsi pakati pa amitundu, ndiye Khritsu mwa inu,chiyembekezo cha ulemerero." Ndiye tikunenetsa kuti Ulemeleroukudikira onse amene adasankhidwapolandira Ambuye Yesu ngati Mbuye ndi Mpulumutsi wawo ndipo tsiku ndi tsiku akuyendam'chipulumutso ndi chikhulupiriro cha choonadi mwa Mzimu Woyera.

15. Chifukwa chake tsono, abale, chirimikani, gwiritsitsani miyambo imene tinakuphunzitsani kapena mwa mau, kapena mwa kalata wathu.

Paulo pano akulimbikitsa kuti Atesalonikaagwiritsitsezimene adalalikirandikuphunzitsa nthawi imene anali pakati pawo.Kutanthauza kuti mau a Mulungu ndiwo amamangiliraokhulupirira kuti akhazikike.

Wokondedwa anzanga apaulendo, pamene tikamba za kuchirimikatikukamba za kugwiritsitsa osawonjezera kapena kuchotserapa Mau a Mulungu ayi.Paulo akutsimikiza kuti zimene amaphunzitsandikulamula zinali Mau a Mulungu.Tsono Yesu Khristundiye amatipatsa chilimbikitso kudzera mwa Mau a Mulungu.Kuwerenga ndikuphunzira Mau a Mulungu kumatithandiza kutitichirimike pa Mau a Mulungu kuti tisatengeke ndi mphepo yachiphunzitso chachilendo.

16. Ndipo Ambuye wathu Yesu Khristu, ndi Mulungu amene ndi Atate wathu amene adatikonda ife

natipatsachisangalatsochosatha ndi chiyembekezo chokoma mwa chisomo,

17. atonthoze mitima yanu nakhazikitse inu mu ntchito yonse ndi mawu onse abwino.

Mundime ino muli nkhani yakuti, Yesu Khristuamatipatsa chilimbikitso kudzera mwa Mau a Mulungu.Ndiye kuwerenga ndikuphunzira Mau a Mulungu kumatithandiza kutitichirimike pa Mau a Mulungu kuti tisatengeke ndi mphepo yachiphunzitso chirichonse.

Taonani tikamawerenga ndikuphunzira Mau a Mulungu timazindikiramadera amene Ambuye akufuna kuti timutumikire. Tikunenetsa kutiokhulupirira ayenera kukhazikikam'mayendedwe awo komanso mu ntchito ya utumiki.Sikokwanira kunena kuti muli ndi chiyembekezo cha kubwera kwaYesu koma osakonda kuwerenga ndikuphunzira Mau a Mulungu ayi.  Kusawerenga mau a Mulungu kumapangitsaokhulupirira kukhala operewerамugawo la utumiki.  Amene ali ndi chiyembekezo chakubwera kwa Ambuye amakonda kugwira ntchito ya Ambuye.  Amatumikira Ambuye amene akumuyembekeza.  Mwa njira inatikunena kuti kutumikira

ndikuchita zimene Ambuye, ndiye kuti inuyomukuyang'anira kubwera kwake.

Tiyeni titsirize ndi mau akuti, inu ndi ine tiyenera kuchirimika kuti tilandirechitonthozo pochita ntchito ya Ambuye.Koma pamene mudzitonthoza ndi zinthu zapadziko, pali chitsimikizo chonse chakutimudzalirabe, ndipo simudzapezachisangalatso ndi chiyembekezo chokoma mwa chisomo. Ntchito yomwe mumachitayosangalatsa Ambuye yokha ndiyo ingakupatsenichisangalatso chokoma chosatha.Zisangalatso zonse zosachokera ku ntchito yokondweretsa Ambuye zimakhalazakanthawi.Sizichedwakutha ndipo zimabweretsaululu wopanda chiyembekezo. Njira yokhayo yakuti tikakhalem'madalitsondikukhazikikamwachikhupirirondikuchirimi ka mwa Ambuye amene adatikondaifenatipatsachisangalatsochosatha ndi chiyembekezo chokoma mwa chisomo, atonthoze mitima yanu nakhazikitse inu mu ntchito yonse ndi mawu onse abwino.

Pezanichitonthozom'Mau a Mulungu kudzera mwa Mzimu Woyera kuti mukhazikike mu ntchito zabwino zonse,

ndikukulam'chiphunzitso cha Mau a Mulungu.Sikokwanirakungokhulupirachowonadi, kondani chowonadipogwira ntchito potumikira Mulungu mu ntchito zanu zonse.

Kwalerotilekeza pano. Koma timasanthula 2 Atesalonika 2:7-17, m'mene timaona nkhani yakubwera kwa wokana Kristu (Antichrist).

Ambuye akudalitseni inu. Amen!